EXAMINATION NO.: ____________________

# THE MALAWI NATIONAL EXAMINATIONS BOARD

## 2023 PRIMARY SCHOOL LEAVING CERTIFICATE EXAMINATION

# CHICHEWA

(Malikisi 100)

**Subject Number: P032**

**Thursday, 11 May** **Time Allowed: 2 h 15 min**

**1 :00 – 3 :15 pm**

**Dzina lanu:** ________________________________________

**Dzina la sukulu yanu:** ________________________________

**Malangizo:**

1. **Onetsetsani kuti pepala ili lili ndi masamba osindikizidwa khumi ndi awiri.**
2. Pepala ili lili ndi magawo anayi: **Gawo A, B, C** ndi **D.**
3. Lembani **dzina** lanu ndi **dzina la sukulu** yanu pamwamba pa tsamba lino.
4. Lembani nambala ya mayeso pamwamba pa tsamba lililonse.
5. Lembani chimangirizo kapena kalata mu **Gawo A** ndipo muyankhe mafunso onse mu **Gawo B, C** ndi **D**.
6. Muchitebulo chili pambalichi onetsani funso lililonse lomwe mwayankha pochonga mubokosi lomwe lili kutsogolo kwake.
7. Perekani kwa oyang'anira kulemba mayeso **(imvijireta)** pepala lonseli nthawi ikakwana.

| Funso | Chongani zomwe mwayankha | Muno musalembemo | |
|---|---|---|---|
| 1 | | | |
| 2 | | | |
| 3 | | | |
| 4 | | | |
| 5 | | | |
| 6-10 | | | |
| 11-15 | | | |
| 16-20 | | | |
| 21-25 | | | |
| 26-30 | | | |
| 31-35 | | | |
| 36-40 | | | |
| 41-45 | | | |
| | | | |

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

©2023 MANEB Onani paseri

## **Gawo A** (Malikisi 30)

**Langizo:** Yankhani funso **limodzi lokha** mwa mafunso awiri ali m'munsiwa. Sankhani chimangirizo **kapena** kalata. Mawu a chimangirizo chanu **kapena** kalata yanu asachepere **100** koma asabzole **150.**

**1.** Lembani chimangirizo pa mutu uwu:

**MWAMBO WOBZALA MITENGO**

Mwa zina tsatani izi polemba:

**Ndime yoyamba**

- tsiku lomwe mwambowo udachitika
- nthawi ndi malo komwe mwambowo udachitikira

**Ndime yachiwiri**

- magulu awiri a anthu odziwika omwe adali nawo pa mwambowo
- mtundu umodzi wa mitengo yomwe idabzalidwa
- mmene mitengo yobzalidwayo idzasamalidwire

**Ndime yachitatu**

- kufunika kobzala mitengo **(Malikisi 30)**

## **KAPENA**

**2.** Lembani kalata kwa amalume anu yopempha ndalama zoti mukalipire kusukulu ya sekondale yomwe mwasankhidwirako.

Mwa zina tsatani izi polemba:

**Ndime yoyamba**

- cholinga cha kalata yanu
- dzina la sekondale sukulu yomwe akusankhiraniko
- tsiku lotsekulira sukulu

**Ndime yachiwiri**

- ndalama zomwe zikufunika kusukuluko
- zinthu zomwe makolo anu akwanitsa kupeza
- kufunika kwa thandizo lomwe mukupempha

**Ndime yachitatu**

- chisangalalo chanu pakupezeka kwa thandizo la ndalamazo **(Malikisi 30)**

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

## Gawo B (Malikisi 20)

## KUMVETSA NKHANI

**Werengani nkhani yotsatirayi mosamala kwambiri kenaka yankhani mafunso otsatirawo pa mizere ili pansi pa funso lililonse.**

Pa sukulu yotchedwa Bwemba, ophunzira ambiri sankamvetsetsa za ufulu wachibadwidwe ndi udindo wawo. Iwo ankatengera zinthu pamgong'o pochita china chilichonse angafune ponena kuti ndi ufulu wawo. Aphunzitsi awo adayesetsa kuwaunikira ophunzirawo kuti alidi ndi ufulu wochita zinthu zomwe akufuna. Komanso adawalangiza udindo waufulu wosiyanasiyana. Iwo adawalangizanso kuti yense wophwanya lamulo amalandira chilango choyenerana ndi lamulo lomwe waphwanyalo. Komabe sizidaphule kanthu kwa ophunzirawo.

Aphunzitsi ataona kuti ophunzira ena akuchitabe zosokoneza mu dzina la ufulu wawo, adakonza msonkhano wa ophunzira onse. Iwo adaitanitsa mkulu woona za ufulu wachibadidwe m'deralo, Bambo Khudzumule. Pa tsiku la msonkhanolo, Bambo Khudzumule adabwera ndi gulu lawo la zisudzo lomwe lidaonetsa sewero lophunzitsa ufulu wachibadwidwe. Mukufotokoza kwawo a Khudzumule, mosapsatira mawu adati ufulu ulipo wosiyanasiyana monga: wokhala ndi moyo, wophunzira, woyankhula zakukhosi, wotetezedwa ku nkhanza ndi wokhala m'mabungwe.

Pamapeto pake adawafotokozeranso za udindo womwe uli pa ufulu wosiyanasiyana. Bambo Khudzumule adatsindika pa udindo wa ufulu wophunzira ndi ufulu wotetezedwa ku nkhanza. Iwo adati ufulu wophunzira, udindo wake ndi kuwerenga, kusajomba kusukulu, kulemekeza aphunzitsi ndiponso kusamalira zipangizo zophunzirira. Kenako adaomba mkota ndi udindo wa ufulu wotetezedwa ku nkhanza kuti ayenera kunena kwa akulu kapena kupolisi ngati achitiridwa nkhanza.

Mafunso akupitirira/…

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

3. **(Continued)**

Kuchokera tsikulo, ophunzira a pasukuluyi adamvetsetsa ufulu ndi udindo wawo. Adasiya mtudzu womwe ankachitira aphunzitsi moti padali mgwirizano wabwino pakati pawo.

a. Ndani adali ndi vuto losamvetsetsa za ufulu wachibadwidwe ?

____________________

**(Malikisi 1)**

b. Fotokozani chomwe chimachitika munthu akaphwanya lamulo.

____________________

____________________

**(Malikisi 2)**

c. Lembani ufulu wachibadwidwe **uwiri** womwe watchulidwa m'nkhaniyi.

(i) ____________________

(ii) ____________________

**(Malikisi 2)**

d. Kodi Bambo Khudzumule adali yani?

____________________

____________________

**(Malikisi 2)**

e. Perekani njira **ziwiri** zomwe zidagwiritsidwa ntchito pophunzitsa ophunzira za ufulu ndi udindo wawo.

(i) ____________________

(ii) ____________________

**(Malikisi 2)**

f. Kodi ophunzira ayenera kuchita chiyani akachitiridwa nkhanza? Perekani mfundo **ziwiri**.

(i) ____________________

(ii) ____________________

**(Malikisi 2)**

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

TECNO SPARK

3. (Continued)

g. Lembani zotsatira **ziwiri** za msonkhano womwe udachitika pa sukulu ya Bwemba.

(i) ____________________

(ii) ____________________

**(Malikisi 2)**

h. Perekani mawu ofanana m'matanthauzo ndi awa:

(i) mtudzu ____________________ **(Malikisi 1)**

(ii) adasiya ____________________ **(Malikisi 1)**

(iii) kujomba ____________________ **(Malikisi 1)**

i. Perekani matanthauzo a zining'a izi:

(i) mosapsatira ____________________ **(Malikisi 1)**

(ii) adaomba mkota

____________________ **(Malikisi 1)**

j. Perekani maphunziro **awiri** omwe akupezeka m'nkhaniyi.

____________________

____________________

**(Malikisi 2)**

**Gawo C** (Malikisi 10)

Yankhani mafunso onse **awiri** m'gawoli.

4. Werengani kankhanika ndipo muyankhe mafunso otsatirawo.

Andireya : Odi! Odi!
Gwadani : Ee! Fikani bambo. Khalani pa chikopapo. Nanga n'kwabwino?
Andireya : N'kwabwino. Dzana kachipsolopsolo kanga kadali kwa Chilanda komwe kadapezako kamsoti. Tamva kuti kamsotiko n'kanu.



Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

4. **(Continued)**

**Mafunso**

a. (i) Ndi malonje anji aperekedwawa?

______ **(Malikisi 1)**

(ii) Kodi Andireya ndi ndani m'malonjewa?

______ **(Malikisi 1)**

(iii) Mawu woti 'kachipsolopsolo' akutanthauzanji?

______ **(Malikisi 1)**

b. Perekani njira **ziwiri** momwe tingasamalire madzi.

(i)

______ **(Malikisi 1)**

(ii) ______ **(Malikisi 1)**

5. **Kupanga ziganizo**

Pangani ziganizo zomveka bwino ndi mawu awa:

a. jeda

______ **(Malikisi 1)**

b. mkoko

______ **(Malikisi 1)**

c. pa

______ **(Malikisi 1)**

d. osati

______ **(Malikisi 1)**

e. pambana

______ **(Malikisi 1)**

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

Mafunso akupitirira/…

## Gawo D (Malikisi 40)

Zungulizani lembo lokhoza **(A, B, C** kapena **D)** m'mafunso otsatirawa.

**Mafunso 6 mpaka 10:** Sankhani mitundu ya mawu omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

**6.** Chimwemwe adali wosayendayenda.
- A. mneni
- B. mlowam'malo
- C. mlumikizi
- D. dzina

**7.** Haa! Mayi anga abwera.
- A. mvekero
- B. mfuwu
- C. mperekezi
- D. muonjezi

**8.** Phwando litatha onse adabwerera kwawo.
- A. mneni
- B. muonjezi
- C. mfotokozi
- D. mvekero

**9.** Ine ndakhala nanu pafupifupi chaka chonse.
- A. mfotokozi
- B. mperekezi
- C. mlowam'malo
- D. dzina

**10.** Khala apa n'kutsine khutu.
- A. mneni
- B. muonjezi
- C. mfotokozi
- D. mlowam'malo

**Mafunso 11 mpaka 15:** Sankhani mitundu ya afotokozi omwe ali ndi mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

**11.** Aphunzitsi awa amaphunzitsa bwino.
- A. waumwini
- B. wochuluka
- C. wamaonekedwe
- D. woloza

**12.** Anthu ambiri afika kumsika.
- A. wochuluka
- B. waumwini
- C. wamgwirizano
- D. wamaonekedwe

**13.** Munthu amene waphedwayo ngosalakwa.
- A. wamaonekedwe
- B. waumwini
- C. wamgwirizano
- D. wamakhalidwe

**14.** Mbuzi yofuntha ija yabedwa.
- A. wamakhalidwe
- B. wamaonekedwe
- C. wamgwirizano
- D. waumwini

**15.** Khasu lalitali lija lathyoka.
- A. wamgwirizano
- B. waumwini
- C. wamakhalidwe
- D. wamaonekedwe

Mafunso akupitirira/…

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

**Mafunso 16 mpaka 20:** Sankhani mawu otsutsana m'matanthauzo ndi omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

**16.** Inu ndi ana aulesi.
- A. olimbikira
- B. amasewera
- C. achidwi
- D. ankhanza

**17.** Atate adavala malaya okongola.
- A. adachotsa
- B. adavula
- C. adayanika
- D. adayalula

**18.** Anyamata amanga mpanda.
- A. akonza
- B. akhulula
- C. apakasa
- D. amasula

**19.** Iye wabweretsa zoperewera.
- A. zakale
- B. zokwanira
- C. zochuluka
- D. zamakono

**20.** Ife tasamba madzi otentha.
- A. ajuu
- B. ozizira
- C. owotcha
- D. owira

**Mafunso 21 mpaka 25:** Sankhani chiganizo chomwe chili ndi zizindikiro zoyenera za m'kalembedwe m'ziganizo zotsatirazi.

**21.**
- A. Kodi, odwala tiziwasamalira motani?
- B. Kodi odwala tiziwasamalira motani?
- C. Kodi odwala, tiziwasamalira motani?
- D. Kodi odwala; tiziwasamalira motani?

**22.**
- A. nchifukwa chiyani anthu amanyoza anzawo?
- B. "Nchifukwa chiyani anthu amanyoza anzawo?"
- C. N'chifukwa chiyani anthu amonyoza anzawo?
- D. n'chifukwa chiyani anthu amanyoza anzawo?

**23.**
- A. Aphunzitsi anena kuti tisalongololе.
- B. Aphunzitsi anena, kuti tisalongololе.
- C. "Aphunzitsi anena" kuti tisalongololе.
- D. "aphunzitsi anena kuti tisalongololе."

**24.**
- A. M'kazi wanga, mwana wamwini ndi gaga saundika.
- B. Mkazi, wanga mwana wamwini ndi gaga saundika.
- C. "Mkazi wanga mwana wamwini ndi gaga saundika".
- D. Mkazi wanga, mwana wamwini ndi gaga saundika.

Mafunso akupitirira/…

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

25. A. Aaa, mwabwera nokhanokha?
B. Aaa! Mwabwera nokhanokha?
C. Aaa? Mwabwera nokhanokha.
D. Aaa! Mwabwera nokhanokha?

**Mafunso 26 mpaka 30:** Sankhani mitundu ya alowam'malo omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

26. Kwathu kuli nkhuku zinayi.
A. waumwini
B. woloza
C. wofunsa
D. wamgwirizano

27. Agwira zochepa lero.
A. wamgwirizano
B. wowerengera
C. wochuluka
D. waumwini

28. Ugule mango asanu kuti tidye.
A. wochuluka
B. wamgwirizano
C. woloza
D. wowerengera

29. Kodi mukufuna ichi ?
A. waumwini
B. woloza
C. wofunsa
D. wamgwirizano

30. Iye wapambana mayeso.
A. waumwini
B. wadzina lakelake
C. woloza
D. wamgwirizano

**Mafunso 31 mpaka 35 :** Sankhani matanthauzo a mikuluwiko yotsatirayi.

31. Padakafunda padajiwitsa galu.
A. Kukonda kukhala malo amodzi.
B. Si bwino kukhalitsa pamalo.
C. Kukomedwa pochita zinthu kumapezetsa mavuto.
D. Si bwino kumapanga zinthu mwaulesi.

32 Fisi akagwa m'mbuna sayankhula.
A. Munthu akagwera m'dzenje sayankhula.
B. Munthu akapezeka akuchita cholakwika sayankhula.
C. Munthu akapezeka ali ndi zabwino sayankhula.
D. Munthu yemwe ali ndi chimwemwe sayankhula.

33. Mphungu sataya nthenga.
A. Munthu wadyera.
B. Munthu wodzikonda.
C. Munthu womana.
D. Munthu wabodza.

34. Madzi akataika sawoleka.
A. Ndikovuta kuwolera madzi akataika.
B. Zinthu zina zikalakwika sizingakonzekenso.
C. Zinthu zikasowa sizingapezekenso.
D. Kutaya mwayi wopezapeza.

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com

Mafunso akupitirira/…

**35.** Chalaka nyani chili ndi khambi.
- A. Chomwe walephera munthu wodziwa palibe angathe.
- B. Chomwe chakanika wamkulu mwana sangachithe.
- C. Chomwe chakanika mphunzitsi ophunzira sangachithe.
- D. Chomwe wamkulu watola mwana sangatole.

**Mafunso 36 mpaka 40:** Sankhani mitundu ya nthambi za ziganizo zosaima pazokha zomwe zatsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

**36.** Iwo andiona pomwe ndimatuluka m'nyumba.
- A. yamfotokozi
- B. yadzina
- C. yoyima payokha
- D. yamuonjezi

**37.** Namwino uja adafotokoza monga ankadziwira.
- A. yadzina
- B. yamfotokozi
- C. yoyima payokha
- D. yamuonjezi

**38.** Akugona kuti apume.
- A. yamuonjezi
- B. yoyima payokha
- C. yamfotokozi
- D. yadzina

**39.** Uyu ndi munthu amene timamufuna.
- A. yadzina
- B. yamuonjezi
- C. yoyima payokha
- D. yamfotokozi

**40.** Iyi ndi nthawi yomwe timalemba mayeso.
- A. yoima payokha
- B. yadzina
- C. yamuonjezi
- D. yamfotokozi

**Mafunso 41 mpaka 45:** Sankhani mitundu ya mayina omwe atsekedwa mzere kunsi kwawo m'ziganizo zotsatirazi.

**41.** Iye adagwa pa mpando.
- A. losakhudzika
- B. lamwinimwini
- C. launyinji
- D. lokhudzika

**42.** Chisomo ndi mtsikana wanzeru.
- A. lamwinimwini
- B. lokhudzika
- C. lopanda mwinimwini
- D. losakhudzika

**43.** Ana awa akusowa chisamaliro cha amayi awo.
- A. lokhudzika
- B. lamwinimwini
- C. losakhudzika
- D. lopanda mwinimwini

**44.** Kupewa matenda n'kwabwino.
- A. lamwinimwini
- B. losakhudzika
- C. lopanda mwinimwini
- D. lokhudzika

**45.** Tiyeni tinyamule mtolo wankhuni.
- A. lamwinimwini
- B. lokhudzika
- C. launyinji
- D. losakhudzika

## MAFUNSO ATHERA APA

**NB: Pepala ili lili ndi masamba osindikizidwa khumi ndi awiri.**

Downloaded for FREE from www.kizitochikuni.com - For more info: contact@kizitochikuni.com